# PHUNZIRO LA 29

1. Kodi a Isirayeli anaŵakhulupilira mawu a Mulungu amene IYE anamuwuza Mose?
-Inde.

2. Ngati ife sitikuŵakhulupilira mawu  a Mulungu, ndiye kuti ife tikumutcha Mulungu kuti ndiwotani?
-Wabodza.

3. Kodi Mulungu adzaŵapulumutsa anthu amene sa-kuŵakhulupilira mawu a Mulungu?
-Iyayi.

4. Kodi Farawo anayankha kuti chiyani pamene Mose ana-muwuza iye kuti Mulungu akumulamula iye kuti aŵalole a Isirayeli kuti adzipita?
-Farawo anati, “Sindikuŵadziŵa AMBUYE, ndipo sindiŵalo-la a Isirayeli kuti adzipita.”

5. Kodi Mulungu anadziŵa kuti Farawo sakaŵalola a Isireyeli kutuluka m’dziko lake la Ejipito?
-Inde.
-Mulungu amadziŵa china chilichonse ngakhale chisanachi-tike.

6. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaganiza zowonetsa mphamvu zake zambiri kwa Farawo pamodzi ndi a Isirayeli?
-Kuti adziŵe kuti Iye yekha, ndiye Mulungu weniweni.

7. Kodi Mulungu anawonetsa bwanji mphamvu Zake zambi-rizo kwa a Ejipito ndi a Isirayeliwo?
-Mulungu anatumiza milili yambiri kwa Farawo ndi a Ejipito

8. Kodi milili imeneyo inali yiti?
-Mulungu anasandutsa madzi a mu mtsinje wa Nayilo ku-

khala magazi.
-Mulungu anatumiza achule kuti aŵavutitse a Ejipito.

-Mulungu anatumiza nthata kuti ziŵalume a Ejipito.
-Mulungu anatumiza mizaza kuti iŵalume a Ejipito.

-Mulungu anapha nyama zonse za a Ejipito.
-Mulungu anatumiza zithupsa kuti ziŵapweteke a Ejipito.

-Mulungu anatumiza matalala, mphenzi ndi mabingu kuti ziwononge zomera ndi mbewu zonse za a Ejipito.
-Mulungu anatumiza dzombe kuti liwononge mbewu zonse za a Ejipito.

-Mulungu anatumiza mdima kuti a Ejipito asathenso kuwonana ndi kuwonanso chinthu china chili chonse.

9. Kodi Farawo ankati chiyani pa nthaŵI iliyonse imene Mulungu amatumiza mulili?
-Farawo ankamuwuza Mose kuti iye aŵalola a Isirayeli kuti adzipita akachotsa muliliwo.

10-Kodi Farawo ankachita chiyani pa nthaŵI iliyonse imene Mulungu amachotsa muliliwo?
-Farawo ankakana kuŵalola a Ejipito kuti adzipita.

11. Kodi chifukwa chiyani milili yonseyi siyimafika ku malo amene a Isirayeli amakhala?
-Chifukwa chakuti Mulungu anamulonjeza Aburahamu, Isaki ndi Yakobo kuti adzaŵadalitsa, ndipo adzaŵasandutsa kukhala mtundu wotchuka ndipo wawukulu.
-Chifukwa chakuti Mulungu ankamuwonetsa Farawo, a Ejipito pamodzi ndi a Isirayeli, kuti Iye yekha ndiye Mulungu, ndipo palibenso wina.

12-Kodi chidzachitike ndi chiyani kwa anthu amene akulimbana ndi Mulungu?



okoma mtima, ndipo anthuwo adaŵapatsa a Isirayeli zonse zimene ankapempha. Chomcho A Isireyeli adalandako chuma cha a Ejipito.

-Usiku omwewo, Farawo anamuyitana Mose ndikuŵalora a Isirayeli kuti adzipita.

-Farawo ankaganiza kuti angathe kulimbana ndi Mulungu.
-Farawo ankaganiza kuti angathe kulimbana ndi Mulungu ndikumugonjetsa Mulunguyo.

-Satana nayenso ankaganiza kuti angathe kulimbana ndi Mulungu ndikumugonjetsa Mulunguyo.

-Palibe amene angathe kumugonjetsa Mulungu.
-Palibe amene angathe kuyiletsa ntchito ya Mulungu.

-Mulungu adzaŵapulumutsa anthu amene akutsata njira ya Mulungu.
-Mulungu adzaŵawononga anthu amene akutsata njira zawo.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 12:51

51-Pa tsiku lomwelo ndi pamene AMBUYE anaŵatulutsa a Isirayeli ku Ejipito mwa magulumagulu awo.

-Mulungu anasunga lonjezo Lake ndipo anaŵatsogolera a Isirayeli potuluka mu Ejipito.

-Kodi Farawo angalimbane ndi Mulungu ndikupambana?
-Iyayi.

-Kodi pali amene angalimbane ndi Mulungu ndikupambana?
-Palibe.

-A Isirayeli anali ana a Adamu ndi Hava ngati m'mene analilinso a Ejipito.

-A Isirayeli anabwadwila m'machimo ngati m'mene analilinso a Ejipito.

-A Isirayeli anachimwa ndipo ankayenera kulandira chilango ngati m'mene analilinso a Ejipito.

-Mulungu anaŵapulumutsa a Isirayeli chifukwa cha chisoni chake chokha.

-Aliyense ali opulumutsidwa chifukwa cha chisoni cha Mulungu chokha.

-Mwana wa chisamba wa Farawo ndi ana achisamba onse a a Ejipito ataphedwa, kodi Farawo anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 12:31-36

31-Usiku omwewo Farawo adayitana Mose ndi Aroni, ndipo adaŵalamula kuti, "Inu pamodzi ndi a Isirayeli onse, fulumirani, mutuluke. Asiyeni anthu anga, pitani mukaŵapembedze AMBUYE monga mudanenera.
32-Mutenge nkhosa zanu, mbuzi zanu, ndi ng'ombe zanu zomwe, monga momwe mudanenera. Ndipo muchoke. Mukapemphere kuti nanenso andidalitseko."
33- A Ejipito adaŵafulumizitsa anthu kuti achoke m'dzikomo, namanena kuti, "Tifatu tonsefe."
34-Chomcho anthuwo adanyamula pa mapewa awo ufa okandiratu wa mkate osathira chofufumitsira, pamodzi ndi mbale zokandiramo mkate zili zokulunga mu m'nsalu.
35-Ndiponso a Isireyeli anali atachita monga momwe Mose adaŵawuzira. Adapempha kwa a Ejipitowo zozikongoletsera za siliva ndi za golide, ndiponso zovala.
36-AMBUYE adaŵasandutsa a Ejipito aja kuti akhale



-Mulungu adzaŵawononga iwowo.

-Ngakhale kuti Mulungu anatumiza milili yowopsa ngati imeneyi kwa Farawo ndi a Ejipito, Farawo ankakanabe kuŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

-Kodi Mulungu anadziŵa kuti Farawo saŵalola a Isirayeli kuti adzipita?
-Inde.

-NthaŵI zonse Mulungu ankadziŵa kuti Farawo saŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

-Ngakhale pa nthaŵI imene Mulungu asamuyitane Mose kuti aŵatsogolele a Isirayeli, Mulungu ankadziŵa kuti Farawo sadzaŵalola a Isirayeli kuti adzachoke m'dziko lake.

-Mulungu amadziŵa china chilichonse chisanachitike..

-Kodi Farawo angalimbane ndi Mulungu ndikupambana?
-Iyayi.

-Kodi pali amene angalimbane ndi Mulungu ndikupambana?
-Palibe.

-Kaya anthu atalankhula zotani, sangathe kuyiletsa ntchito ya Mulungu.

-Kaya anthu angachite zotani, sangathe kuyiletsa ntchito ya Mulungu.

-Mulungu akaganiza zichita china chake, nthaŵI zonse amachimaliza.

-Mulungu atumizanso mulili wina omaliza , ndipo Farawo aŵalola a Isirayeli kuti adzipita.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 11:1

1-Ambuye anamuwuza Farawo kuti, “Tsopano ndimupatsa chilango chimodzi Farawo pamodzi ndi a Ejipito onse. Pambuyo pa chilango chimenechi, adzakulolani kuti muchoke. Ndiponso adzachita chokupilikitsani kuti muchoke, osabwerelanso.”

-Kodi mulili womaliza umene Mulungu atumize ukhala otani?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 11:4-7

4-Tsopano Mose adamuwuza Farawo kuti, “AMBUYE akunena kuti, “Ndiyenda pakati pa a Ejipito pakati pa usiku,
5-ndipo mwana aliyense wachisamba adzaphedwa mu Ejipito monse muno. Kuyambira mwana wa chisamba wa Farawo, amene ali oyenera kuloŵa ufumu, adzaphedwa, mpaka mwana wa chisamba wa mdzakazi amene akupera pa mphero. Mwana woyamba kubadwa wa zoŵeta adzafanso.
6-M’dziko lonse la Ejipito mudzakhala maliro okhaokha amene sadawonekenso nkale lonse, ndipo sadzawonekanso.
7-Koma pakati pa a Isirayeli, ndi galu yemwe sadzawuwa munthu kapena choweta china chilichonse, kuti mudziwe kuti AMBUYE amasiyanitsa pakati pa a Ejipito ndi a Isirayeli.

-Mulili womaliza umene Mulungu adzatumize ndi wakupha ana onse amuna oyamba kubadwa a a Ejipito ndi nyama zomwe.

-Chifukwa chakuti mulili womalizawo unali owopsa kwambiri, Mulungu anaŵawuza a Isireyeli kuti awukonzekere



-Inde.

-Chilango cha Mulungu pa tchimo ndi imfa.
-Mulungu adzapereka chilango pa machimo onse.
-Mulungu adzapereka chilango cha imfa pa machimo onse.

-Mulungu akaganiza zopereka chilango pa tchimo , palebe amene angapulumuke.

-Kodi panali mwana wa chisamba aliyense wa a Isirayeli amene anaphedwa?
-Panalibe.

-Kodi chifukwa chiyani panalibe mwana wa chisamba wina aliyense wa a Isirayeli amene anaphedwa?

-Chifukwa chakuti a Isirayeli anamumvera Mulungu ndipo anapaka magazi pamwamba pa chitseko ndi pa mphuthu ziŵiri za chitsekocho.

-Ngati m’mene mwana wa nkhosa wabwino kwambira anafera m’malo mwa Isaki, chomchonso mwana wa nkhosa kapena wa mbuzi wabwino kwabiri anafa m’malo mwa ana achisamba a a Isirayeli.

-Chifukwa chakuti a Isirayeli anamumvera Mulungu, Mulungu anasunga lonjezo lake ndipo anazipitilira nyumba za a Isirayeli.

-Kodi Mulungu amachita zimene walankhula nthaŵI zonse?
-Inde.

-Mulungu analikumbukira lonjezo lake loŵatsogolera a Isirayeli potuluka ku Ejipito mu ukapolo.

-Mulungu analikumbukira lonjezo lake lotumiza Mpulumutsi kupitira mwa Aburahamu ndi a Isirayeli.

mbuzi odwala kuti apereke msembe, Mulungu anakamupu-lumutsa iye?
-Iyayi.

-Kodi mu Isirayeli anakangomangilira mwana wa nkhosa kapena mbuzi pafupi ndi nyumba yake, osamupha, kodi Mulungu anakampulumutsa iye?
-Iyayi.

-Mwana wa nkhosa kapena mbuzi ankayenera kuti afe.
-Magazi a nkhosa kapena mbuzi ankayenera kuti atuluke.

-Mulungu sankafuna kuti a Isirayeli ayiŵale kuti chilango cha Mulungu pa tchimo ndi imfa basi.

-Kodi chinachitika chiyani usiku umenewo?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 12:29-30

29-Pakati pa usiku, AMBUYE adapha ana onse achisamba m'dziko la Ejipito. Adayambira mwana wa chisamba wa Farawo amene ankayembekezera kuloŵa ufumu wake, mpaka ana a akayidi a m'nyumba za m'dima za m'ndende. Ana onse oyamba kubadwa a nyama adaphedwanso ndithu.
30-Farawo ndi nduna zake zonse, pamodzi ndi a Ejipito onse, adadzuka pakati pa usiku, ndipo m'dziko lonse la Ejipito munali maliro okhaokha, chifukwa chakuti panalibe banja limene linalibe mwana wakufa.

-Mwana wa chisamba wa Farawo ndi ana achisamba onse a a Ejipito anamwalira.

-Ana oyamba kubadwa onse a nyama za Farawo ndi za a Ejipito onse anaphedwa.

-Kodi Mulungu anaŵapha ana achisamba onse a a Ejipito?



muliliwo.

-Chifukwa chakuti mulili womalizawo unali owopsa kwambi-ri, izi ndi zimene Mulungu anaŵawuza a Isirayeli kuti azich-ite kuti ana awo amuna oyamba kubadwa asamwalire.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 12:1 ndi 3-5

1-AMBUYE analankhula kwa Mose ndi Aroni m'dziko lija la Ejipito kuti,
3-Mulengeze kwa khamu lonse la a Isirayeli kuti pa tsiku lakhumi la mwezi uno, munthu aliyense adzasankhire banja lake mwana wa khosa mmodzi. Banja lililonse li-dzatenge mwana wa nkhosa mmodzi.
4- Banja likachepa, kuti silingathe kudya nyama yon-seyo, mabanja aŵiri oyandikana aphatikizane pamodzi, monga momwe aliri anthu, tsopano onsewo adyere limodzi. Mulinganiziretu chiŵerengero cha anthu odya nyamayo, modziŵa mmene munthu m'modzi angadyere.
5-Mwana wa nkhosa wake adzakhale opanda chilema, wa mphongo, wa chaka chimodzi. Mungathe kusankhanso mwana wa mbuzi.

-Mulungu analamula kuti mamuna okwatira aliyense wa m'banja lililonse la a Isirayeli, asankhe mwana wa mphon-go wa nkhosa kapena mbuzi wa chaka chimodzi.

-Mulungu analamulanso kuti mwana wa chaka chimodzi wa mphongo wa nkhosa kapena mbuziyo akhale wopanda chilema china chilichonse.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu analamulanso kuti mwana wa chaka chimodzi wa mphongo wa nkhosa kapena mbuziyo akhale wopanda chilema china chilichonse?

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wabwino kwambiri.
-Chifukwa chakuti chilichonse chimene amalankhula

Mulungu chimakhala chabwino kwambiri.
-Chifukwa chakuti china chilichonse chimene Mulungu amachita chimakhala chabwino kwambiri.

-Mulungu anakalora mwana wa nkhosa kapena mbuzi wa mphongo wa chaka chimodzi ndipo opanda chilema yekha basi.

-Mulungu sadzayilora msembe yodwala.
-Mulungu sadzayilora msembe yovulala.

-Kodi mukumukumbukira mwana wa nkhosa amene anakodwa ndi nyanga zake mchithukuluzi kuti alowe m'malo mwa Isaki uja?

-Kodi chifukwa chiyani mwana wa nkhosayo anakodwa ndi nyanga zake?

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wabwino kwambiri.
-Mulungu adzalora msembe yabwino kwambiri yokha.

-Ngati a Isirayeli akufuna kuti apulumutsidwe ku imfa, ayenera kuŵatsatira mosamalira malamulo amene analamula Mulungu.

-Iwo anakangosankha mwana wa nkhosa kapena mbuzi wa mphongo wa chaka chimodzi ndipo opanda chilema.

-Kodi china chiyani chimene Mulungu anaŵalamula a Isirayeli kuti achite?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 12:6

6-Mumusunge mpaka pa tsiku la 14 la mwezi, pamene khamu lonse la a Isirayeli lidzaphe nyama zawozo madzulo ndithu.



Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 12:12-14

12-Usiku umenewo, Ine ndidzapita m'dziko la Ejipito ndipo m'dziko lonselo ndidzapha ana onse oyamba kubadwa, a anthu ndi a nyama omwe. Ndidzalanga milungu yonse ya Ejipito. Ine Ndine AMBUYE.
13-Magaziwo adzakhala chizindikiro pa nyumba zimene mumakhalamo. Ndikadzangowona magaziwo, ndidzakupitilirani inuyo, ndipo mulili wosakaza siwudzakugwerani, pamene ndidzakanthe dziko la Ejipito.
14-"Tsiku limeneli mudzidzalisunga. Tsiku limeneli mudzidzalikumbukira, ndipo mudzidzachita chikondwerero, kupembedza AMBUYE. Mibado yonse izidzakumbukira tsiku limeneli, kuti likhale lamulo lamuyaya, lakuti muzidzachita chikondwerero pa tsiku limenelo."

-A Isirayeli akadzaŵamvera malamulo a Mulungu, kodi Mulungu analonjeza kuti adzachita chiyani?
-Mulungu ananalonjeza kuti mulili omalizawo siwudzafika kwa iwowo, ndipo ana awo achisamba amuna sadzamwalira.

-Kodi a Isirayeli anamumvera Mulungu?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 12:28

28-A Isirayeli adapita, ndipo adamvera zimenezo. Adachitadi zonse zimene AMBUYE adalamula Mose ndi Aroni.

-A Isirayeli anachita zonse ngati m'mene Mulungu anaŵalamulilila iwowo.

-A Isirayeli anachita zonse zimene Mulungu anaŵalamula kuti azichite.

-Kodi mu Isirayeli anakasankha mwana wa nkhosa kapena

m'mene anaŵalamulilila IYE.

-Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli ankayenera kuti achite zonse ngati m'mene Mulungu anaŵalamulilila?

-A Isirayeli anakapanda kuchita zonse ngati m'mene Mulungu anaŵalamulilila, ndiye kuti muliliwo unakafika kwa iwowo, ndipo ana awo amuna achisamba anakamwalira.

-Mulungu anakaŵapulumutsa ana achisamba a a Isirayeli, a Isirayeliwo anakachita zonse ngati m'mene Mulungu anaŵalamulilila.

-Mulungu anakaŵapulumutsa ana achisamba a a Isirayeli, a Isirayeliwo anakatsata njira ya Muklungu yokha.

-Mulungu sadzaŵalora anthu kuti adzipulumutse okha mu njira zawo.

-Kodi chinachitika ndi chiyani pamene Adamu ndi Hava anatsatira njira yawo ndi kudzipangira okha zovala za masamba?
-Mulungu anazikana zovala zawozo.

-Kodi chinachitika ndi chiyani kayini atatsata njira yake ndikukana kupereka msembe ngati m'meme Mulungu analankhulira?
-Mulungu anayikana msembe ya Kayini.

-Njira ya Mulungu ndi njira yokhayo imene idzatipulumutse ife.
-Tikapanda kutsata njira ya Mulungu, Mulungu adzatikana ife.

-Kodi Mulungu anaŵalonjeza chiyani a Isirayeli, a Isirayeliwo akadzamumvera IYE?



-Mulungu anaŵalamula a Isirayeli kuti asunge ana a nkhosawo kapena mbuzi mpaka pa tsiku la 14 la mwezi.

-Pa tsiku la 14 la mwezilo, Mulungu anaŵalamula a Isirayeliwo kuti adzaphe ana a nkhosawo madzulo a tsiku lomwelo.

-Mulungu analamula kuti mwana wa nkhosa aphedwe.
-Mulungu analamula kuti mwana wa nkhosa afe.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu analamula kuti mwana wa nkhosa afe?

-Uku kunali kuŵakumbutsa a Isirayeli kuti chilango cha Mulungu pa tchimo ndi imfa.

-Adamu ndi Hava asanachimwe, panalibe imfa pa dziko la pansi pano.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anachimwa, imfa inabwera pa dziko la pansi.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anachimwa, imfa imafika kwa anthu onse.

-Mulungu anaŵalamulanso a Isirayeli kuti atsile magazi a mwana wa nkhosa kapena mbuziyo m'mbale.

-Ngati a Isirayeli akufuna kuti apulumutsidwe ku imfa, ayenera kuŵatsatira mosamalira malamulo amene analamula Mulungu.

-Ndipo anayenera kupha mwana wa nkhosa kapena wa mbuzi wa chaka chimodzi wa mphongo, wopanda chilema, ndikutsira magazi ake m'mbale.

-Kodi kenako Mulungu anaŵalamula a Isirayeli kuti achite nawo chiyani magaziwo?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 12:7

7-Tsopano adzatengeko magazi a nyamayo ndi kuwaza pa mphuthu ziŵiri za chitsekozo, ndi pamwamba pa chitseko cha nyumba imene akadyeremo nyamayo.

-Mulungu anaŵalamula a Isirayeli kuti adzatengeko magazi a nyamayo ndi kuwaza pa mphuthu ziŵiri za chitsekozo, ndi pamwamba pa chitseko cha nyumba imene akadyeremo nyamayo usiku umenewo.

-Anali magazi a nyama amene anakatha kuŵapulumutsa a Isirayeli ku chilango cha Mulungu.

-Ngati a Isirayeli akufuna kuti apulumutsidwe ku imfa, ayenera kuŵatsatira mosamalira malamulo amene analamula Mulungu.

-Chimene anakachita ndikungotenga magazi a nyamayo ndi kuwaza pa mphuthu ziŵiri za chitsekozo, ndi pamwamba pa chitseko cha nyumba imene akadyeremo nyamayo usiku umenewo.

-Kodi china ndi chiyani chimene Mulungu anaŵalamula a Isirayeli kuti achite?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 12:22b

22-AMBUYE anati, Munthu aliyense asakatuluke mnyumba mwake mpaka m'maŵa."

-Mulungu anaŵalamula a Isirayeli kuti munthu aliyense asakatuluke mnyumba zimene zinali ndi magazi m'makomo mwakemo mpaka m'maŵa."



-A Isirayeli ankayenera kuti akhale nkati mwa nyumba zimene zinali ndi magazi kunja kwake.

-Magazi amene anali panjawo, ankaŵavundikira a Isirayeli amene anali mkati aja.

-Imfa ya mwana wa nkhosa kapena mbuzi kunja kwa nyumbazo, imkaŵavundikira a Isirayeli amene anali mkati mwa nyumbazo.

-Ngati a Isirayeli akufuna kuti apulumutsidwe ku imfa, ayenera kuŵatsatira mosamalira malamulo amene analamula Mulungu.

-Chimene anakachita, ndikungokhala mkati mwa nyumba imene inali ndi magazi pa chitseko chake mpaka m'maŵa.

-Kodi china ndi chiyani chimene Mulungu anaŵalamula a Isirayeli kuti achite?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 12:46b

46-AMBUYE anati, "Ndipo musaphwanye mafupa ake."

-Mulungu anaŵalamula a Isirayeli kuti asaphwanye fupa lina lililonse la mwana wa nkhosa kapena mbuzi.

-Ngati a Isirayeli akufuna kuti apulumutsidwe ku imfa, ayenera kuŵatsatira mosamalira malamulo amene analamula Mulungu.

-Chimene anakachita ndi kusaphwanya fupa lina lililonse la mwana wa nkhosa kapena mbuzi.

-Mulungu anaŵawuza a Isirayeli kuti achite zonse ngati